

**Maphunziro**

a

**Alangizi othandizira  
alimi a ziweto m'midzi**

**Ziweto  
kwa anthu**

Small Scale Livestock and Livelihoods Program

PO Box 1604, Lilongwe Malawi



## Ziweto kwa anthu

### **Phunziro 1: Ntchito ya Ziweto**

**Zolina za phunziroli:**

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:

1. Kudziwa ndi kufotokoza kufunika kwake kosunga ziweto
2. Kufotokoza phindu lake mokhudzana ndi ndalamu ndi chuma chokhudza moyo wa munthu zomwe zimadza kuchokera kuziweto
3. Kufotokoza zonse zoyenera kuchita posamala ziweto kuti zikhale zathanzi

### **Yankhani mafunso awa:**

Kodi ndiphindu lanji lomwe limapezeka posunga ziweto?

Nanga ntchito ya ziweto ndi chiani?

Ntchito yeniyeni ya ziweto ndi chiani?

Chiweto	Ntchito zake
Ng'ombe	Ngati mosungira ndalamu Kulowolera mkazi Nyama Zikopa/zikumba Mkaka Kulimira ndi kukoka ngolo Manyowa othira kumbewu za m'munda
Abulu	Kulimira ndi kukoka ngolo Ena amadya nyama yake Manyowa othira kumbewu za m'munda
Mbuzi	Ngati mosungira ndalamu Kulowolera mkazi Nyama Zikopa/zikumba Mkaka

Chiweto	Ntchito zake
<b>Nkhumba</b>	Ngati mosungira ndalama Nyama Manyowa othira kumbewu za m'munda
<b>Nkhosa</b>	Ngati mosungira ndalama Nyama Zikopa/zikumba Manyowa othira kumbewu za m'munda
<b>Nkhuku</b>	Ngati mosungira ndalama Mazira Nyama Manyowa othira kumbewu
<b>Abakha</b>	Ngati mosungira ndalama Mazira Nyama Manyowa othira kumbewu
<b>Akalulu</b>	Ngati mosungira ndalama Nyama
<b>Agalu</b>	Kuteteza katundu Kusaka /liwamba lanyama za m'thengo Oyenda/kukhala ndi mbuyache
<b>Amphaka (pusi)</b>	Kudya ndi kuthawitsa makoswe Oyenda/kukhala ndi mbuyache

### **Yankhani mafunso awa:**

Fotokozani ntchito ya zinthu zimene zimachokera ku ziweto. Nanga m'dera lanulo mumagwiritsa ntchito yanji zinthu zochokera kuziweto?

1. Nyama ya ng'ombe: Imadyedwa kuti ndinso pakakhaka zochitika zanji? Nanga ndalama zimene zapezeka pogulitsa nyama zimakhala zandani? Ndalamazo amagwiritsa ntchito yanji?
2. Nyama ya mbuzi, yankhumba, kapena ya nkhosa: Imadyedwa kuti ndinso pakakhala zochitika zanji? Nanga ndalama zimene zapezeka pogulitsa nyama zimakhala zandani? Ndalamazo amagwiritsa ntchito yanji?
3. Mkaka wa ng'ombe (kapena wa mbuzi): Kodi umangomwedwa kumudzi komweko kapena amagulitsako?
4. Zikopa zang'ombe ndi zambuzi: Kodi amazitani zikopa zimenezi? Kodi mwini wake amalandirapo malipiro pazikopa

zimenezi?

5. Nyama ya nkhuku: Kodi nyama ya nkhuku imadyedwa kumakomoku kapena amakonda kugulitsa ndi ndalama?
6. Mazira: Kodi mazira amadyedwa kunyumba kapena amakonda kugulitsa pofuna ndalama?
7. Ziweto zogwira ntchito: Kodi abulu kapena ng'ombe zokoka ngolo kapena zolimira amagwiritsira ntchito ndi mwini wake yekha? Kodi amalipiritsa ngati anthu ena abwerekwa ziweto zogwira ntchitozi? Ngati amalipiritsa, kodi malipiro ake amakhala aphindu?

Tafotokozani za mitengo ya ziweto. Kodi mitengo ya ziweto zathanzi ngati izi, ili motani m'dera lanulo?

- Ng'ombe yamkaka yachaka chimodzi
- Ng'ombe yachikuda (Malawi Zebu) yachaka chimodzi
- Mtheno wogwira ntchito yokoka ngolo kapena kulimira
- Mbuzi yaikazi ya chaka chimodzi
- Nkhumba yaikazi ya chaka chimodzi
- Msoti wankhuku wotetera

## Zofunikira pantchito yoweta ziweto zathanzi

### **Yankhani mafunso awa:**

Fotokozani kufunikira kwa zinthu zoyenera pakawetedwe kaziweto zathanzi poganzira zamtundu wachiweto monga nkhuku kapena mbuzi ndi zina zotero. Fotokozani za khola loyenera, chakudya ndi kadyetsedwe kabwino ndi zina zotero.

<b>Khola</b>	Likhale labwino lotha kuteteza ziweto ku chisanu yozizira kapena mphepo ya mkuntho, kudzuwa, kapena kuzirombo zolusa.
<b>Chakudya ndi kadyetsedwe</b>	Kuti chiweto chikule bwino ndi kuswana koyenera, pafunika zakudya zamagulu ndi zokwana.
<b>Kuchulukitsa (kuswanitsa)</b>	Kusankha ziweto zoyenera ndiponso zathanzi zoti zikhale m'gulu loswanitsa.
<b>Kuteteza kumatenda</b>	Kuteteza kumatenda kuti ziweto zisafe ndinso kuti zikhale zathanzi, zokula bwino ndi kuswana bwino.

***Yankhani mafunso awa:***

Sankhani mtundu wina uli wonse wachiweto ndipo fotokozani m'mene khola labwino lingapangitsire kuti chiweto chimenechi chikhale chathanzi.

Fotokozani njira zakadyetsedwe kabwino kamene kangapangitse kuti chiweto chanu chikhale ndi moyo wathanzi.

## **Phunziro 2: Kudziwa ziweto zathanzi ndi chodwala**

**Zolinga za phunziroli:**

**Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:**

- 1. Kudziwa ndi kufotokoza kusiyana kwa kaonekedwe kachiweto chathanzi ndi chodwala**
- 2. Kuyesa kutentha kwathupi lachiweto pogwiritsa ntchito choyesera chotchedwa mercury thermometer**
- 3. Kufotokoza zizindikiro zamatenda a chiweto chimene chikudwala ndikutha kupereka uthenga (lipoti) mwaukadaulo wokhudza matenda amene akuganizira kuti abuka m'deralo**
- 4. Kumvetsa ndi kufotokoza zam'mene nthenda ya chiwewe imafalikira, m'mene chiweto chodwala chiwewe chimaonekera ndinso kuteteza kwake kwa chiwewe**

- Dzwani kuti mutha kuona zizindikiro za chiweto chathanzi kapena chodwala mutaima patali.
- Musaiwale kuima patali mukafuna kuona zizindikiro za umoyo wa chiweto chanu posafuna kuchisokoneza kapena kuchidzidzimutsa.

**Yankhani mafunso awa:**

Sianitsani zizndikiro za chiweto chathanzi ndi zizndikiro za chiweto chodwala.

Muyende m'mudzi m'mene akuwetamo ziweto zamitundu yosiyanasiyana. Onetsetsani ziwetozo ndipo muftokoze m'mene ziwetozo zikuonekera thanzi lamatupi ake, ndi umoyo wake.

Monga mwaukatswiri wanu, ngati mwaona chiweto chimene chikuoneka ngati chikudwala, uzani anzanuwo zizndikiro zamatenda amene mukuganiza kuti chiwetochi chikudwala molingana ndi zizndikiro zimene mwaonazo.

	<b>Chiweto chathanzi</b>	<b>Chiweto chodwala</b>
<b>Kaonekedwe</b>	Kuchangamuka, kuchita zonse bwino	Kuombwa, kutopa, osatekeseka, kudakukhos, kudzipatula pazinzake ndi kukanika kudzuka.
<b>Ubweya</b>	Wosalala, wowala	Wonyankhalala, wotuwa
<b>Pamphuno / pakamwa</b>	Ponyowa koma osati kuchita dovu kapena mamina	Pouma kapena kutuluika dovu mowirikiza ndi mosayenera
<b>Konekedwe kathupi</b>	Lowoneka bwino, lonenepa, losalala, (ng'ombe zamkaka zimakhala zoonderapo pamene zangoswa ndipo zikukamidwa)	Zoonda, kamimba kouma, yowonetsa mafupa (msana, nthiti, nyung'unyu) (Chioneni ndi kuchisisita chiweto chanu)
<b>Nthenga</b>	Zosalala ndi zowala bwino	Zonyankhalala
<b>Ndowe/zitosi</b>	Zolimba bwino, osasiya nsete kumchiraku	Mpwerere (madzimadzi), zoura (kutupidwa/kudzimbida). Kupakika ndowe kum'chiraku.
<b>Miyendo</b>	Yamphamu ndi yoyima bwino	Yofoka, yamatewe, yokhota, yopunduka, yotupa mu akakolo ndi m'mabondo.
<b>Chikopa / chikumba</b>	Chosalala, chowala	Chozomokazomoka choipa, zotupatupa, chamkupe.
<b>Mkaka wa ng'ombe</b>	Woyela, wonunkira bwino, wopanda misere	Wamiselemisele, wophatikizika ndi magazi, wowoneka ngati mafinya (chikasu), fungo loyipa.ndi wamadzimadzi.
<b>Ziboda</b>	Zooneka bwino, zamphamu	Zotalika kwambiri, zokhota
<b>Kakulidwe/ kaperekedwe ka mkaka/kaikiridwe kamazira, kukhala ndi nyere ndi kaswanidwe</b>	Zokula bwino ndi mofulumira, zopereka mkaka ndi kuikira mazira moyenera, zimachita nyere pa masiku ake ndi kuswa nthawi yoyenera	Kupinimbira, mkaka/mazira wochepa kapena osaperekanso, sichita nyere moyenera ndipo siziswana panthawi yake.
<b>Kutentha kwa thupi</b>	Koyenera (onani m'bokosi lili m'musili)	Kokwera, nthawi zina kutsika pansi kwambiri


## Kuyesa kutentha kwa thupi la chiweto (pogwiritsa ntchito mercury thermometer)

### **Ntchito:**

Werengani pa mercury thermometer m'mene ikuonetsera kutentha kwake nthawi imeneyo. Aliyense awerenge pa mercury thermometer mobwerezabwereza(katatu kapena kasanu) mpaka atadziwa. Ngati ndi nkotheka yesani kutentha kwathupi la chiweto ndipo muone kutentha kwake pa mercury thermometer. Lembani dzina kapena chizindikiro chachiwetochi ndi tsiku limene mwachiyesalo mongoyerekeza ngati mukuchitadi zenizeni.

### **Kayesedwe kake**

- Musanayambe kuyesa, onetsetsani kuti mwakutumula mercury thermometer yanu kuti mercury ikhale pamalo oyenera m'mene kukutenthera kunjaku. Lowetsani mercury thermometer mkatikati mwakonyerera kwa chiweto. Onetsetsani kuti mercury thermometer yakhudza m'mbali mwathumbo osati mundowe. Kuti mercury thermometer isatuluke kapena kuphwanyika, muigwiritse ndithu pamene mwalowetsa mwa nthawi yokwana mphindi imodzi. Chotsani, pukutani ndipo werengani kutentha kwathupi pa mercury thermometer.
- Nthawi zonse mukumbuke kulemba kutentha kwathupi, dzina kapena chizindikiro cha chiweto ndi tsiku; kuti alangizi ena a za ziweto adzathe kuwerenga atabwera pakholapo.



Kuyesa kutentha kwa thupi la ng'ombe  
(Courtesy FAO "A manual for the primary animal health care worker")

### Kutentha kwathupi koyenera kwa ziweto zosiyanasiyana za thanzi (°C)

Chiweto	Kutentha koyenera (°C)
Cattle Ng'ombe	38.5
Thole	39.5
Mbuzi	39.5
Nkhosa	39
Bulu	38.2
Nkhumba	39
Mwana wankhumba	39.8
Nkhuku	42

Nthawi zina kutentha koyenera kukhoza kukwera kapena kutsika ndi 1 °C.

### Kufotokoza matenda a ziweto

#### *Yankhani mafunso awa:*

Fotokozani zam'mene zikuonekera ziweto zodwala zimene mwaziona. Mutha kupereka lipoti lotani kwa alangizi a za ziweto ku boma? Ndi nfundu ziti zimene ndi zoyenera kumuaza mlangizi wa za ziweto wa boma pa zamatenda a ziweto amene mukuchita report.

Fotokoza bwino zonse zokhudza mlili wa matenda a ziweto omwe abuka m'dera lanu. Lembani pa fomu ya lipoti mwa ndondomeko yonse za matenda amenewo ngati kuti akubuka nthawi imeneyo.

- Pamene muona kuti chiweto chikuonetsa zizindikiro zamatenda, muyenera kupereka zonse zimene mwaziona zoyenera kunena mu lipoti yanu kuti akatswiri akuthandizani moyenerera. Sizothandiza kungolemba/kunena kuti chiweto chikudwala kapena kuti chiweto chafa basi. Perekani zizindikiro zonse zomwe mwaziona.
- Ena mwamafunso omwe muyenera kuyankha ndi awa: mukhozanso kufunsa mwiniwake ziwetozo kuti akuthandizeni kuyankha ena mwa mafunsowa.
  - Ndi ziwo ziti zimene zikudwala? Mtundu wanji waziweto? Ndi za msinkhu wotani? Ndi zazimuna kapena zazikazi? Nanga zikuoneka bwanji thupi lake?
  - Nanga zizindikiro zamatendawa zimaoneka bwanji? Chiweto chimaoneka bwanji?
  - Matendawa amatenga nthawi yitali bwanji chiweto chisanachire?
  - Nanga zafa ziwo zingati?
  - Ndi ziwo zingati zimene zikudwala?
  - Ndi ziwo zingati zimene sizikudwala?
  - Matendawa adayamba liti?
  - Nanga matendawa agwa m'dera liti? Kodi agwa khola limodzi kapena m'makola ambiri?
  - Kodi anayeserako kuchita njira zotetezera kapena kuchiritsa matendawa? Ngati ndi choncho, ndi njira ziti?
  - Thandizo limene likufunika ndilotani pofuna kuteteza kapena kuchiritsa matendawa?
  - Nfundo ina ili yonse yomwe ingakhale yothandiza?

### **Lipoti lokhudza matenda a chiweto**

- Fomu ili kuseli kwa pepapala lino ndi loperekera uthenga wa matenda a chiweto
- Pamene alangizi othandizira alimi a ziwo m'midzi aona kuti ziwo zikudwala, alembe uthenga kwa alangizi pa mafomu amenewa.
- Mafomu awa atha kugawidwa kwa alangizi onse othandizira alimi a ziwo m'midzi.
- Pamene kwagwa matenda alangizi othandizira alimi a ziwo m'midzi alembe pa mafomu amenewa mwachangu ndikuwatumiza kwa alangizi a za ziwo a boma.

## Fomu/chikalata yolembapo lipoti la matenda a ziweto

Anthu am'dera amene aphunzitsidwa za umoyo wa ng'ombe ndipo akugwira ntchito yothandiza ulangizi wa ziweto, azilemba mofulumira pachikalata ichi zizindikiro zonse zamatenda ndi zina zonse zofunikira pa za chiweto chimene akuchiganizira kuti chikudwala. Tumizani msanga kwa alangizi a za ziweto.

Dzina la olemba lipoti:	
Tsiku:	
Mudzi/dera:	
Telefoni ngati ali nayo pafupi (Dzina la mwini foni):	

Mtundu wa ziweto zimene zikudwala? <b>(zungulizani pa mtundu wa chiweto)</b>	Ng'ombe	Mbuzi	Nkhumba	Nkhuku	Zina (chulani)
Zamsinkhu wanji?	Zazikulu zikulu		Ana		Za misinkhu yonse
Zamatupi wooneka bwanji?	Zooneka bwino		Zosaoneka bwino		Maonekedwe ena aziweto
Bvuto kweni kweni ndi chiani? Zikuonetsa zizindikiro zanji? Ziweto zikubvutika bwanji?  <b>(Ngati malo olembaachepta pitirizani kuseliku)</b>					
Zizindikiro zamatendawa zinayamba liti?					
Ndi ziweto zingati zafa?					
Ndi ziweto zingati zikudwala?					
Ndi ziweto zingati sizikudwala?					
Ndi dera liti limene lakhudzidwa ndi matendawa? Kodi ndi khola limodzi kapena dera lalikulu?					
Matendawa amatenga nthawi yaitali bwanji?					
Kodi pali ziweto zomwe zabwera kuchokera kwina kapena zomwe zapita kudera lina kuchokera m'khola kapena m'dera lomwe mwagwa matenda? Ndi liti ndipo ndi zingati?					
Kodi anayeserako kuchita njira zotetezera kapena kuchiritsa matendawa? Ngati ndi choncho, ndi njira ziti?					
Thandizo limene likufunika ndilotani pofuna kuteteza kapena kuchiritsa matendawa?					
Nfundu ina iriyonse yomwe ingakhale yothandiza?  <b>(Ngati malo olembaachepta pitirizani kuseliku)</b>					

### **Phunziro 3: Matenda odziwika ndi woopsyia - Chiwewe**



**Zolina za phunziroli:**

**Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe kumvetsetsa:**

- 1. Chomwe chimayambitsa matenda a chiwewe**
- 2. Momwe matenda a chiwewe amafalitsidwira**
- 3. Zizindikiro zomwe chiweto chodwala chiwewe chimaonetsa**
- 4. Kuteteza matenda a chiwewe**

#### **Yankhani mafunso awa:**

Kodi matenda a chiwewe mumawadziwa?

- Chimayambitsa matenda a chiwewe ndi chiyani?
- Ndi mtundu wa ziweto ziti umene ungadwale matenda a chiwewe?
- Kodi ndi mtundu wa ziweto zonse umene ungaethe kupatsira munthu matenda a chiwewe?
- Nanga munthu atha kutenga matenda a chiwewe kuchokera kuti?
- Kodi galu wodwala chiwewe amaonetsa zizindikiro zotani?
- Kodi choyenera kuchita ndi galu amene akuonetsa zizindikiro zoti akudwala chiwewe ndi chiyani?
- Kodi choyenera kuchita ndi Ng'ombe kapena mbuzi imene ikuonetsa zizindikiro zoti ikudwala chiwewe ndi chiyani?
- Nanga tichite chiyani ndi munthu amene walumidwa ndi nyama imene ikuonetsa zizindikiro zoti ikudwala chiwewe?

- Kodi pamatenga nthawi yayitali bwanji kuti galu amene walumidwa ndi galu wachiwewe kuti ayambe kuonetsa zizindikiro zoti akudwala chiwewe?
- Pamatenga nthawi yaitali bwanji kuti galu afe pomwe wayamba kuonetsa zizindikiro zoti akudwala chiwewe?
- Tingachiritse bwanji matenda a chiwewe?
- Tingateteze bwanji matenda a chiwewe?

- Matenda achiwewe amakonda kugwira agalu, afisi ndi nyama zina za mtchire. Matendawa athanso kugwira mitundu ina ya ziweto ndi nyama zina. Munthu amatha kutenga ndi kudwala matenda a chiwewe. Koma matenda a chiwewe sagwira nkhuku ndi mtundu wina uli wonse wa mbalame.
- Matendawa ndi oopsa kwambiri akagwira galu kapena fisi chifukwa nyama zimenezi zitha kuluma munthu ndi kumupatsira matendawa.
- Chiwewe chimayamba ndi kachirombo kosaoneka ndi maso kotchedwa virus. Ka chilombo kamene ka kamakalowa m'bongo ndi ku uononga ndipo nyama siithanso kudya kapena kumwa madzi. Kawirikawiri, matendawa amachititsa kuti nyama ikhale yolusa. Agalu ndi afisi amaluma agalu anzawo, kapena anthu ngakhale chinthusa chilichonse angakumane nacho. Saopanso munthu ayi. Ng'ombe ndi mbuzi nazonso zimalusa ndipo zimangoliralira kumapanga phokoso lambiri.
- Nyama yodwala chiwewe itha kufalitsa matenda a chiwewe poluma inzake. Kachirombo koyambitsa matenda a chiwewe kamapezekwa m'malovu a nyama yomwe ikudwala chiwewe ndipo ikaluma nyama ina, kamalowa pachilondapo kudzera m'malovumo. Ka chilomboka sikangathe kulowa m'thupi kudzera pakhungu lopanda chilonda. Palibe choopsyamunthu kukhudza nyama yodwala chiwewe - koma choopsa ndikuti ikulume.
- Koma sikuti nyama ili yonse yoluma ndi yodwala chiwewe ai. Ngati galu wayamba kuonetsa zizindikiro za chiwewe, ayenera kufa pasanathe masiku khumi. Koma ngati apitirira masiku khumi ali ndi moyo chilumirenimunthu, ndiye kuti alibe chiwewe.
- Munthu kapena nyama siyamba kudwala chiwewe nthawi yomweyo imene yalumidwa ndi gali /chiweto cha chiwewe ayi. Pamatenga milungu iwiri kapena miyezi ingapo kuti zizindikiro zamatenda a chiwewe ziyambe kuoneka.
- **Galu** amaonetsa zizindikiro izi akamadwala matenda a chiwewe:
  - Amasinha makhalidwe ake, amachita khalidwe lachilendo

- Amasiya kudya ndi kumwa madzi komwe, ngakhale amafunitsitsa kumwa koma amalephera kumeza madziwo.
- Nthawi zambiri amalusa ndi kuyamba kuluma nyama zina kapena zinthu zina kapenanso anthu. Nthawi zina amangokhala oziya ndi kungokhala chetete koma osatseka kukamwa.
- **Ng'ombe, Nkhosa** kapena **Mbuzi** zimaonetsa zizindikiro izi zikamadwala matenda achiwewe:
  - Chiweto sichikhala chokhazikika ndipo chimakhala chochangamuka mopitirira muyeso.
  - Zimadziluma ndipo chimatulutsa dovu mowirikiza kuchokera kukamwa.
  - Chiweto chimaliralira ndi mau a chilendo mosokosa kwambiri.
  - Chiweto chimafa ziwalo ndipo pomaliza chimafa.
- Zimene tingachite ndi galu woluma:
  - Kumbukira kuti si agalu onse oluma amene akudwala matenda achiwewe
  - Ngati galu ali ndi mwini wake, mumufunse khalidwe latsiku ndi tsiku lagalu wakeyo. Kodi khalidwelo lasintha modabwitsa tsopano? Ngati pali kusintha kwa khalidwe, muganizire kuti galuyo akudwala chiwewe.
  - Ngati galuyo akuonetsa zizindikiro zamatenda achiwewe, adziwitseni alangizi a za ziweto mwamsanga. Galuyo aphedwe ndithu. Ngati waluma munthu, alangizi a za ziweto amulembere kalata yopita nayo kuchipatala kuti akabayidwe katemera woteteza matenda a chiwewe.
- Zimene tingachite ngati chiweto chiri kuonetsa zizizndikiro za kuti chikudwala matenda a chiwewe:
  - Ngati ziweto monga ng'ombe kapena mbuzi imene inalumidwa ndi nyama yodwala chiwewe iyamba kuonetsa zizindikiro za kuti yayamba kudwala chiwewe, iphedwe ndi kukaikwira padzenje. Simungatenge matenda pakudya nyama yophikidwa bwino ya chiweto chomwe chafa ndi matenda a chiwewe. Koma mutha kutenga matenda a chiwewe pamene malovu ndi madzi ena a m'thupi la nyamayo alowa m'thupi lanu podzera m'mabala amene angapezeke m'manja pokonza nyamayo.
- Kodi matenda a chiwewe atha kuchiritsidwa?
  - Ayi. Nyama yomwe ikudwala matenda a chiwewe singatheke kuchiritsidwa. Ngati chiweto chayamba kuonetsa zizindikiro zoti chikudwala matenda a chiwewe, chikufa ndithu. Ngati pali anthu amanena kuti ali ndi mankhwala ochiritsira matenda a chiwewe, ndi abodza amenewo.
  - Tengerani kuchipatala mwachangu munthu amene walumidwa ndi nyama yodwala matenda a chiwewe.

- Kodi titha kuteteza ziweto ndi anthu kumatenda a chiwewe?
  - Inde. Izi zitha kutheka pokhapo chiwetocco **chisanalumidwe**. Nyama ya mtundu wina uli wonse itha kulandira katemera woteteza matenda a chiwewe. Ndikofunikira kwambiri kutemera agalu chifukwa ndi woopsy a kwa anthu. Mukhoza kutemera ziweto zina monga ng'ombe, kapena mbuzi pokhapokhapo ngati pali chiopsezo choti zilumidwa ndi nyama zodwala chiwewe.

## **Phunziro 4: Ntchito za alangizi othandiza pakasungidwe ka ziweto m'midzi**

**Zolina za phunziroli:**

**Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe kumvetsa:**

1. Za munthu wothandizira ulangizi wa ziwetoyu ndi wotani.
2. Udindo ndi ntchito zake za munthu ameneyu ndi zotani
3. Kodi munthu atha kumalipiridwa motani, ndipo mtengo wa mankhwala ndi katemera uzikhala wotani
4. Kodi zoyenereza munthu ameneyu kuti asankhidwe ndi gulu kuti akaphunzitsidwe ndikugwira ntchito imeneyi ndi zinthu ziti
5. Udindo ndi ntchito za anthu awa mu ulimi wa ziweto ndi wotani:
  - **Mlimi/ Mwini ziweto**
  - **Othandizira ulangizi wa ziweto ku midzi**
  - **Mlangizi wa za ziweto**

### **Kodi wathandizira ulangizi wa ziweto ndi ndani?**

- Munthu wothandizira ulangizi wa ziweto wakudera ndi munthu wakuderako amene wasankhidwa ndi kuperhunzitsidwa za kasamalidwe kabwino kaziweto kuti akathandize alimi aziweto m'dera lakelo njira zabwino zowetera ziweto za thanzi, zokula bwino ndiponso zopindilutsa. Maina ena a anthu amenewa ndi M'langizi woona ndi kuperhunzitsa za ziweto za thanzi m'mudzi / m'dera,
- Anthu amenewa amalipidwa ndi mwini wake wa ziweto zimene wakazipatsa mankhwala kapena katemera. Akhozanso kumalipidwa ndi gulu la alimi aziweto. Malipro akhoza kukhala ndalamaka kapena katundu.
- Alangizi amenewa ndi ololedwa kugula, kugulitsa ndi kumwetsa ziweto mankhwala motsatira malamulo a bungwe la Pharmacy, Medicines and Poisons Board ndi Dangerous Drugs Act. Alangizi amenewa ndi ololedwa kupindula pamtengo omwe amagulitsira mankhwala kapena katemera kuti azitha kumagula ndi kusunga mankhwala abwino nthawi zonse.
- Alimi kapena magulu a ziweto sali oumirizidwa kugwiritsa ntchito alangizi othandizirawa ngati sakufuna.

### **Kusankha anthu ofuna kukhala alangizi aza ziweto othandizira a m'madera**

- Anthu akuderalo ndi amene ali ndi mphamvu zosankha munthu amene adzakhale mlangizi wa za ziweto wothandizira.

- Pofuna kufupikitsa nkhani, akomiti ya gulu la ziweto makamaka azimai ndiwo apatsidwe mphamvu zosankha munthu amene adzakhale mlangizi wa za ziweto wothandizira.
- Akomiti akhazikitse ndondomeko zoyenera kulondola posankha munthu amene adzakhale mlangizi wa za ziweto wothandizira.
- Zina zofunika kuika m'ndondomeko imeneyi zalambedwa pansipa.
- Akomiti ayenera kugwirizana ndi fundo zonse zoikika m'ndondomeko zosankhira munthu amene adzakhale mlangizi wa za ziweto wothandizira.

### **Ndondomeko yofunika kutsata posankha munthu amene adzakhale mlangizi wa za ziweto wothandizira**

Munthu wofuna kukaphunzira akhale:

- Wokhulupirika: akhale wokhulupirika ndiponso waulemu wake m'deralo. Akhale wokhulupirika pankhani ya ndalama.
- Wodzipereka: azipezeka nthawi zonse, akhale ofuna kuthandiza anthu a m'dera lake. Asakhale wotangwanikwa ndi ntchito zina.
- Wodalirika: akhale munthu wachidziwitso m'zinthu zambiri ndi wachidwi pofuna kutukula ulimi wa ziweto. Ndipo akhale woti ulimi ndiyo ntchito yake.
- Akhale woti atha kumapita yekha m'makola kuyendera ndi kupereka mankhwala kuziweto.
- Akhale wodziwa kuwerenga ndi kulemba (kuti azitha kulemba zochita ndi ma lipoti) ndi kutha kachita masamu amuyeso woperekera mankhwala.
- Akhale nzika ya m'deralo.
- Akhale wotha kugwirira ndi kukhalirana bwino ndi a langizi a za ziweto ndi atsogoleri amagulu a za ziweto m'deralo.
- Anthu adzivomereza kugwira ntchitoyi mongodzipereka osayembekezera cholowa chilichonse kuchokera kumabungwe omwe akugwira ntchito yachitukuko cha ulimi wa ziweto m'deralo kapena mabungwe akunja.

## **Udindo ndi ntchito**

### **1. Mlimi mwini ziweto:**

- Mlimi ndiye mwini wake wa ziweto amene amayang'anira ziweto tsiku lili lonse. Udindo wa mlimi ndi:
  - Kudziwa zofuna za ziweto
  - Aonetsetse kuti ziweto zili kupeza chakudya, madzi abwino ndi khola labwino.
  - Kupereka mankhwala amene angathe kuchipatsa chiweto ndi kupereka njira zina zoteteza ziweto kumatenda
  - Kupereka ma lipoti ngati aona zizindikiro zamatenda paziweto zake kwa mlangizi wa za ziweto wothandizira kapena mlangizi wa za ziweto.

### **2. Mlangizi wothandizira wa m'dera:**

- Mlangizi wothandizira ndi wodziwa bwino za ziweto. Atha kulangiza za kasamalidwe kabwino ka ziweto, kudziwa zizindikiro za matenda a ziweto ndi zina zotero. Ndi wophunzitsidwa bwino ndipo ali ndi chidziwitso chabwino pazakawetedwe kaziweto ndipo atha kuthandiza ziweto monga mlimi wabwino waziweto angathere.
- Mlangizi wothandizira wa m'dera: ayenera kalandira malipiro a ntchito yomwe wagwira moyerekeza ndi nthawi, mtunda umene wayenda ndi mtengo wa mankhwala amene wapereka ku chiweto.
- Ngati pali kusagwirizana pamtengo umene wanena, akomiti athandizire kuweruza. Alimi kapena magulu a ziweto sali oumirizidwa kugwiritsa ntchito alangizi othandizirawa ngati sakufuna.
- Udindo wa Mlangizi wothandizira wa m'dera:
  - Kudziwa zonse zokhudza ulimi wa ziweto m'dera lakero mokhudzana ndi kuchuluka kwa alimi a ziweto, mitundu ya ziweto ndi kuchuluka kwake ndi mabvuto amene alimi akukumana nawo pa ulimi wa ziweto.
  - Kuthandizapo pa mavuto amene alimi akukumana nawo.
  - Kupereka mankhwala kuchiweto chimene akuganizira kuti chikudwala malinga ndi kudziwa kwake. Mlangiziyu ayenera kukhala wodziwa za matenda a chiweto monga m'mene mlimi wozindikira amadziwira.
  - Kupereka lipoti kwa mlangizi wa za ziweto wa m'deralo kapena amene ali wofupikira ndi deralo.
  - Kugwiritsa ntchito mankhwala ndi katemera monga omwetsa, obaya ndi nyereti, a m'maso, obaya kunphumbu za mabere, dibi, opopera ndi owaza.

- Mlangizi wothandizirayu sayenera kupereka mankhwala amene amayenera kuperekedwa ndi dokotala wa ziweto yekha kapena mankhwala amene sali kuwadziwa bwino.

### **3. Mlangizi wa za ziweto**

- Mlangizi wa za ziweto ndi wolembedwa ntchito ndi boma ndipo ndiyе ali oyang'anira ntchito zonse za ulimi wa ziweto m'deralo. Udindo wake ndiwo:
  - Kudziwa ndi kumvetsetsa zonse zokhudza ulimi wa ziweto m'mene ziriri m'dera lakero mokhudzana ndi kuchuluka kwa alimi a ziweto, mitundu ndi kuchuluka kwa ziweto, mavuto amene alimi akukumana nao pa ulimi wa ziweto ndi zina zotero.
  - Kupereka mankhwala ndi katemera ku ziweto motsatira malamulo a boma.
  - Kuongolera alangizi othandizira aja pa za ntchito yawo ya ulangizi wa za ziweto.
  - Kukambirana ndi alangizi othandizira aja zofunikira pa zaulimi wa ziweto m'deralo.
  - Kupereka uthenga wa za matenda omwe abuka m'deralo kwa wam'kulu woona za ziweto ku boma.
  - Kuthandizira kupeza mankhwala ndi katemera ofunikira m'deralo.

## **Mafunso apomaliza pa maphunziro a gawo**

1. Kodi alimi amapezamo phindu lanji mu ulimi wa ziweto? Nenani zifukwa zenizeni zimene alimi amasungira ziweto? Poyankha mafunsowa munene zokhudza ziweto za mtundu wa mbuzi ndi nkuku.
2. Kodi zinthu zinayi zofunikira paulimi wabwino ziweto ndi ziti?
3. Lembani zizindikiro za ziweto chathanzi ndi chodwala.
4. Kodi kutentha koyenera kwa thupi kwa ng'ombe, thole, ndi mbuzi za thanzi kumafika pati?
5. Pamene mukuyendera m'makola ndipo mwapeza kuti ziweto zikudwala ndipo mukuganizira kuti kwagwa matenda. Mukulemba lipoti kwa mlangizi wa za ziweto kapena dokotala wa vetenare kuti abwere adzafufuze zamatendawo. Kodi ndi nfungo ziti zomwe mulembe mu uthengawo?
6. Kodi matenda a chiwewe amafalikira bwanji kwa munthu? Kodi kachilombo koyambitsa matenda a chiwewe kamalowera kuti m'thupi?
7. Kodi pamapita nthawi yitali bwanji kuti nyama yomwe yalumidwa ndi nyama yodwala chiwewe kuti iyambe kuonetsa zizindikiro za matenda a chiwewe?
8. Kodi mankhwala ochiritsira matenda a chiwewe ndi chiyani?
9. Kodi mungateteze bwanji ziweto zanu kumatenda a chiwewe?
10. Kodi mlangizi wa za ziweto wothandizira m'dera ndi munthu wotani?
11. Kodi mlangizi wa za ziweto wongothazira m'dera amalipidwa motani?
12. Nenani nfungo zofunikira mndondomeko yosankhira mlangizi wa za ziweto wongothazira m'dera.
13. Nanga udindo wa mlangizi wa za ziweto wongothazira m'dera ndi wotani?